



MUTU 3:

MOSE



1706 B.C.

PA NTHAWI YA NJALA, YAKOBO AMENE ANALI MDZUKULU WA ABRAHAMU, ANATENGA ANA AKE ONSE AAMUNA 12, ANA AO NDI ANTCHITO AO NAPITA KUKAKHALA KU IGUPTO. KU IGUPTOKO, ANACHULLUKANA NGATI MCHENGA WA PA DZIKO LAPANSI.

POSAKHALITSA ANA A YAKOBO, AMENE AMATCHEDWANSO ISRAELE, ANACHULLUKA KUPAMBANA AIGUPTO.



FARAO, MFUMU YA AIGUPTO, ANASANDUTSA AKAPOLO ANA A YAKOBO NDIPO ANAWAUMIRIZA KUGWIRA NTCHITO ZOWAWA; ANKALUMBA NJERWA.

MULUNGU ADAMUZA ABRAHAMU KUTI ANTHU AKE ADZAPITA KU DZIKO LACHILENDO NDIPO KUMENEKO ADZAKHALA AKAPOLO. ADALONJEZANSO KUTI PAKADZAPITA ZAKA 400 ADZALANGA DZIKO LIMENELO NDIPO ADZATULUTSA ANTHU AKE NDI KUWABWEZERA KU DZIKO LA MALONJEZANO.




NDIKUKULUZANI, NDI ZOONA!
FARAO AKUOPA KUTI TACHULUKANA
KWAMBIRI. AKUPHA MAKANDA ONSE.
AIGUPTO NDI OFOOKA KOMANSO
NDI AULESI. ANTHU ANTHU
AMAPIRIRA NTCHITO
ZOLEMETSА. AKUTIOPA.



SADZAPHA MWANA
WANGA. MULUNGU
ADZAMTETEZA.


HA! KODI MULUNGU
ANGACHITE CHIYANI NDI
MPHAMVU ZA FARAO?



**AI! MWANA
WANGA TOTO.
SIMUNGACHI
TE ZIME-
NEZI.**

**FARAO, POOPA KUTI AYUDA
ANKACHULUKANA KWAMBIRI,
ANAGANIZA ZOMAPHA
MAKANDA AAMUNA.**

GENESIS 46:5-7; EKSODO 1:1-12, 22



KOMA AMAI,
NDIDZAWAUZA CHIYANI
ASILIKALI NDI ANZATHU
ENA AKAFUNSA KUTI
KHANDA LATHU
LILI KUTI?

UDZAWAUZE ZOONA
ZOKHAZOKHA. AMAI AKE
ANANTAYA MU MTSINJE
KOTERO KUTI ASILIKALI
SANAMUPHE.

PAFUPIFUPI 1525 B.C.



AMAI, KODI
M'MENEMU
SIMULOWA
MADZI?

TACHIMATA
NDI PHULA.
CHIZIDZAYAN
DAMA.

KODI
TIDZAMUONANSO
MCHIMWENE
WATHUYU? ONANI
AIGUPTOWO!

MULINGU
ADZAMUTETEZA.
IWE UKAKHALE PAFUPI
POMWEPO NDIPO
UZIKAMUYANG'ANIRA.

MWANA WAMKAZI WA FARAO
ANABWERA KUMTSINJEKO
KUDZASAMBA.




TAMVEARNI! NDIKUMVA
KULIRA KUCHOKERA MU
MTANGA LWO!



AYENERA
KUKHALA
MMODZI
MWA ANA
A AHEBRI.


EEE, NDI
WOKONGOL
A ETI?

AYENERA
KUTI ALI NDI
NJALA.




NDIKANAPEZA
WINA WOTI
AZINDIYAMWITS
IRA
NDIKADAMUSUNG
A MWANAYU.

MMODZI MWA
ANA A AHEBRI ALI
PANO. MWINA
MWAKE ANGADZIWE
WINA WOTI
NKUMAYAMWITSA
MWANAYU.



NDIPITA KUTI
NDIKAYESE KUPEZA MAI
AMENE AKHOZA KUYAMWITSA
MWANAYU. NDIKUDZIWA KUTI
PALI WINA AMENE
WANGOTAYA MWANA WAKE MU
MTSINJE. AMENEYO AKANALI
NDI MKAKA WAMBIRI
M'MAWERE AKE.


EKSODO 2:3-9



NDACHITA
CHIYANI? KODI
NDIDZAMUONANSO
MWANA WANGA?
KODI MULUNGU
AMASAMALADI?

MUKANACHITA
CHIYANI?
SIMUKANAMUBISA
MPAKA KALE KALEKALE.
NDITHU, ASILIKALI
AKANAMUPEZA NDI
KUMUPHA. MUYENERA
KUNGOKHULLUPIRIRA
MULUNGU.

**AMAI,
AMAI!**

A comic book panel featuring two women. The woman on the left has long dark hair and is wearing a black and white patterned top. She is speaking with a surprised expression. The woman on the right is shown in profile, with her hand near her mouth as if listening intently. The background is dark with some architectural lines.

AMAI, MWANA WAMKAZI WA FARAO ANABWERA KU MTSINJE NDIPO WAPEZA MCHIMWENE WANGA WAMNG'ONO UJA. AFUNA KUTI MWANAYO AKHALE WAKE, NDIPO AKUFUNA MAI WINA WOTI AZIMUYAMWITSIRA! NDIPO TSOPANO AKUBWERA KUNYUMBA KUNO!

ADALITSIKE MULUNGU WAMUYAYA!



NDAMVA KUTI MWANA
WANU ANAPHEDWA. PEPANI
KWAMBIRI. MWANA UYU NDAMPEZA
MU MTSINJE. MUZINDIYAMWITSIRA
NDIPO NDIDZAKULIPIRANI. //

AKADZALEKA
KUYAMWA NDIDZABWERA
KUDZAMUTENGA NDI KUPITA NAYE KU
NYUMBA YACHIFUMU KUMENAKALEREDWE
KUTI ADZAKHALE FARAO WA DZIKO LA
EJIPITO. TIDZAMUTCHA DZINA
LAKE MOSE.



PAMENE MOSE ANKAKULA, MAI WAKE
UJA ADAMUPHUNZITSA ZA MULUNGU
WOONA WA MAKOLO AKE. MULUNGU
ANALI NDI CHOLINGA CHAPADERADERA
NDI MWANA AMENEYU.



LUMPHIRA
MUNO,
MWANA WA
MFUMU,
TIKUPITA KU
NYUMBA
YACHIFUMU.

KODI
ZIMENEZI
ZIMATHAMANG
A KWAMBIRI
NDITHU?

ZIKOMO KWAMBIRI
CHIFUKWA CHOYAMWITSA
MOSE. AKUONEKA
WATHANZI ZEDI. AKAKULA
ADZAKHALA WAMPHAMVU
NDI WOLEMERA.

EKSODO 2:8-10

MONGA MWANA WONGOMUTOLA WA
MWANA WAMKAZI WA FARAO, MOSE
ATAKULA ANAKHALA MUNTHU
WAMPHAMVU MU IGUPTO. MULLINGU
ADAKONZA KUTI MOSE ADZAKHALA
WAMPHAMVU NDI WACHUMA, KOMA
SANKAIWALA ZAKUTI ANALI MHEBRI.





MOSE,
NDIKUKUZA KUTI
MULUNGU WA MAKOLO
ATHU, ABRAHAMU, ISAKE, NDI
YAKOBO, ADAMUZA
ABRAHAMU KUTI ANA AKE
ADZACHULUKA ZEDI
NDIPO KUTI ADZAKHALA ALENDO
M'DZIKO LA ENI.
NCHIFUKWA CHAKE LERO
TILI MONGA TILILIMU!


INDE, NDIPO
ADAMUZANSO ABRAHAMU
KUTI TIDZAZUNZIDWA
M'DZIKO LIMENELO KWA
ZAKA 400. TAKHALA MUNO
TSOPANO KWA ZAKA 359,
NDIPO KWANGOTSALA ZAKA
41 KUTI TIFIKE PA ZAKA
ZIMENE MULUNGU
ADANENAZO.



ZIONEKA KUTI ZIMENEZI
NDI ZOSATHEKA. FARAO SANGALOLE
KUTI AKAPOLO AKE ONSE ACHOKE,
NDIPO SANGALOLENSO KUTI ACHOKE
NDI CHUMA. KOMA MWINA MWAKE
PALI NJIRA INA. TIKUDIKIRIRANJI
ZAKA 41 KUTSOGOLOKU?



ADAMU ZANSO ABRAHAMU KUTI
ADZALANGA DZIKO LIMENELO CHIFUKWA
CHA ZOIPA ZIMENE ADZATICHITIRA,
NDIPO KUTI TIDZATULUKA M'DZIKOMO NDI
CHUMA CHAMBIRI NDI KUBWERERA KU
DZIKO LIMENE MULLUNGU ADAPERKA
KWA MAKOLO ATHU.



ANA A AHEBRI ANKAZUNZIKA CHIFUKWA CHA
ULAMURIRO WA MABWANA AO. ANKAKUMBA NKHUTI
NDI KUMALIMBA NJERWA. MOSE SANKAKONDWA
POONA ABALE AKEWO AKUZUNZIKA, CHONCHO
ADAGANIZA ZOCHITAPO KANTHU.

DZUKA
ASANAKUMENY
E KUTI LIFE!

DZUKA,
IWE
NKHUMBA
YA LIFE!

MALUME,
DZUKANI.

EKSODO 2:10-11



TSIKU LINA MASANA, MOSE
ANAONA AIGUPTO AKUMENYA
ANTHU AKE MWANKHANZA.

NTHAWI
YAKUOMBOLA
YAFIKA TSOPANO.
ZIMENEZI ZIYENERA
KULEKEKA.



**ZIMENE
ZI AI!**

MOSE ANAPHA MWIGUPTO
NDI KUMUKWIRIRA MU
MCHENGA, KOMA ANTHU ENA
ADAONA ZIMENEZI NDIPO
ADAKAMLUZA FARAO.



**IMA
POMWEPO,
LYENERA
KUKAYANKHA
MLANDU WA
KUPHA.**

**NDI
MOSE!**


**MULLUNGU!
NDACHITIRAN
JI ZIMENEZI?**

PAFUPIFUPI 1491 B.C.



MOSE ANACHOKA KU IGUPTO
NDIPO ANATHAWIRA
M'CHIPULULU. NDIPO ANALI
YEKHA, WOPANDA ABALE NDI
ABWENZI. SADAOMBOLE
ANTHU AKE. ANALEPHERA
KUDZIOMBOLA IYE MWINI.

EKSODO 2:11-15



MOSE ADAKHALA
AKUYENDA KWA
MASIKU AMBIRI.
ATAONA KUTI
SANGAPITIRIRE
ADAFIKA PA
ZITHANDO ZA
ABUSA A ZIWETO.

TAONANI!
MUNTHU!

AKUONEKA
NGATI ALI
PAFUPI KUFA.
BWERETSANI
MADZI.

NDI
MWIGUPTO!

MOSE ADAYAMBA MOYO
WATSOPANO PAKATI PA
AMIDIYANI. ANAPHUNZIRA
MOYO WA M'CHIPULULU,
ANAKWATIRA, NDIPO ANALI
MBUSA WA ZIWETO.
ZAKA 40 ZINAPITAPO NDIPO
ANAYAMBA KUIWALA
ZA KU IGUPTO. MOSE
SANKAYEMBEKEZANSO ZOTI
NKUDZAONANANSO NDI ANTHU AKE.



CHIMENECHI NCHODABWITSA
NDITHU! CHITSAMBA CHIJA
CHAYAMBA KUYAKA BWANJI,
NANGA BWANJI SICHIKUNYEKA?
CHIKUNGOYAKA BASI.





**MOSE, VULA NSAPATO
ZAKO. UKUIMIRIRA PA
MALO OPATULIKA. INE NDINE
MULLUNGU WA MAKOLO AKO,
ABRAHAMU, ISAKE, NDI
YAKOBO.**


**NDAONA MMENE
ANTHU ANGA AKUZUNZIKIRA
KU IGUPTO NDIPO NDAMVA
MAPEMPHERO AO. NTHAWI
YAKWANA YOTI NDIWAOMBOLE
KU MAZUNZO AO NDI
KUWABWERETSA KU DZIKO
LIMENE NDIDALONJEZA
MAKOLO AO.**

**NDITUMA IWE NDIPO
UDZATULUTSA ANTHU ANGA
MU UKAPOLO WAO. UDZAMUUSA
FARAO ZOTI ANTHU ANGA
ATULLIKE, KOMA IYE ADZAKANA.
NDIPO NDIDZAONETSA MPHAMVU
ZANGA KWA AIGUPTO. PAMBLYO
PAKE IYE ADZALOLA KUTI
ANTHU ANGA ATULLIKE.**



KOMA SAKAKHULUPIRIRA
KUTI MWANDITUMA
NDIPO AZIKANGOSEKA.





**PONYA
PANSI NDODO
YAKOYO!**

**CHIYANI?
NDODO YANGA!**





**YASANDUKA
NJOKA
YAULULU
KWAMBIRI!**

**GWIRA MCHIRA
WA NJOKAYO NDIPO
LYINYAMULE.**



**YASANDUKANSO
NDODO YANGA IJA!**



**PITA KU IGUPTO.
NDIDZAKUPHUNZITSA
ZOTI UKAYANKHULE
NDIPO NDIDZAKUWZA
ZOTI UKACHITE.**



EKSODO 4:1-4, 12-16

1445 B.C.

PAPITA ZAKA 40
TSOPANO. ONSE AMENE
ANKADZIWA ZIMENE
NDIDAACHITA
ANAMWALIRA. PALIBE
AMENE
AKANDIZINDIKIRE.

MPAKA
PAMENE FARAO
ADZALOLERE
KUTI ANTHU A
MULLINGU APITE.

UKUBWERERA KU
IGUPTO! KOMA
NANGA AMENE ANKAFUNA
KUKUPHA AJA?

UDZAKHALA
ULI
KUMENECO
MPAKA LITI?





ITANANI AKULLUAKULU
ONSE ASONKHANE PAMODZI!
NTHAWI YOTI ANTHU A
MULLINGU AOMBOLEDWE
YAFIKA!

KODI
AMENEWA
NDANI?

UYO NDI AARONI
MLEVI. WINAYO AKUONEKA
NGATI MMODZI WA IFE,
KOMA SIKAPOLO.



PAMENE FARAO
ADAYAMBA KUPHA ANA
AAMUNA A AHEBRI KUFIKIRA
NTHAWI IYI PATHA ZAKA 80.
MOSE ANADADWA PA
NTHAWI YA ZOKHOMAZO.
AMAI AKE ADAMUBISA KU
MTSINJE MU MTANGA.

FIKANI
PAFUPI, INU
NONSE
AKULLUAKULU
A ISRAELE.


EXODUS 4:29-31



CHIFUKWA CHA CHIKONZERO CHA MULLINGU, MWANA WAMKAZI WA FARAO ADAMUPEZA MOSE KUMENECO NDIPO ANALEREDWA NGATI MWIGUPTO. // ZAKA 40 PAMBUIYO PA IZI, MOSE ADAGANIZA ZOTI AZUNZIKE PAMODZI NDI ANTHU AKE M'MALO MOMALAMULIRA NGATI MWEJIPITO. KWA ZAKA 40, MOSE WAKHALA AKUKHALA M'CHIPULULU CHA DZIKO LIMENE MULLINGU ADALONJEZA MAKOLO ATHU. POSACHEDWAPA MULLINGU WAMUYANKHULA NDIPO WAMUONETSA MMENE ATIOMBOLERE KUCHOKA M'MANJA MWA FARAO! TSOPANO, MOSEYU AKUONETSANI ZIZINDIKIRO ZIMENE ADZAGWIRITSA NTCHITO POTSIMIKIZIRA FARAO ZOTI TITULUKE NDITHU.

MULUNGU WA ABRAHAMU
WANDIYANKHULA KUPYOLERA
M'CHITSAMBA CHOYAKA MOTO
NDIPO WANDITUMA KUTI
NDIKUTSOGOLERENI KU DZIKO
LA MAKOLO ATHU. TAONANI
CHOZIZWITSA ICHI.





**HEYI! NDODO
YAKE
INASANDUKA
NJOKA.**

MUSAOPE



ONANI
ICHI.



TSOPANO TIPITA KWA FARAO!

*INDE, CHIMENECHI
CHIDZACHITITSA DZANZI
FARAO.*

*ICHI
NCHOZIZ
WITSA!*

MULLINGU
WATUMIZA
MPULUMUTSI.

MULLINGU
WA
ABRAHAMU!

EKSODO 4:17, 30


PALIBE CHIMENE
CHASINTHA
M'DZIKO MUNO
CHICHOKERE INE
ZAKA HO ZAPITAZO.
UKUMBUKIRE
KUNENA ZIMENE
NDAKUUZAZI.



MULUNGU WA ISRAELE
WAYANKHULA NDI MOSE. MULUNGU
AKUTI ULOLE KUTI ANTHU AKE
APITE M'CHIPULULU KWA MASIKU
ATATU, KUKAPEMBEDZA NDI
KUKAPEREKA NSEMBE.



HA! MULUNGU WA ISRAELE?
HA HA HA HA, SINDIMDZIWA
MULUNGU WANU. KODI MULUNGU
AMENEYU NDANI KUTI NDIMUMVERE?
ZIMENEZI NDI ZOSEKETSA NDITHU.
SINDIDZALOLA KUTI AKAPOLO
ANGA APITE M'CHIPULULU KWA
MASIKU ATATU.



NDAMVA MMENE IWE
UKUSOKONEZERA ANTHU ANGA,
UKUWAUZA KUTI ALEKE KUGWIRA
NTCHITO. NDIPO TSOPANO AFUNA
ACHOKEPO KWA MASIKU ATATU
KUKAPEMEBDZA MULUNGU AMENE
INE SINDIMDZIWA.
NDIONETSETSA KUTI NTCHITO
YAO IPOSE KALE.


KUCHOKERA TSOPANO
AZIDZIPEZERA OKHA UDZU WOLUMBIRA
NJERWA. TSOPANO CHOKANI
PAMASO PANGA NDIPO BWERERANI
KUMENE MWACHOKERA.

EXODUS 5:1-7



KODI
NKUKHULUPIRIR
A ZOPLUSA
ZOTERE?

ZIMENE ZIJA
NZOSEKETSА. AMABWERA
KUNO NGATI
AKUYANKHULADI MAU A
MULUNGU.




MUKUTIENZA KUTI ZIMENE
INU MWACHITA
NKUTI IFE ATIONJEZERE
NTCHITO? KUOMBOLA
NKUMENEKU? NDIYE
MUKUGANIZA KUTI
MULUNGU ANAKUTUMANI?

KODI IYEU
AKUGANIZA
KUTI NDANI?
KODI
NGOPAMBANA
IFE?

ZACHABE
CHABE!

KOMA
ZOONA NDITHU
ANATIPUSITSA.
TINAKHULUPIRIR
A BODZA LAKE.

MULIBE CHOCHITA ETI?
MUKUFUNA KUTI MUKAPEMBEDZE
MULUNGU WANU. TIKUPHUNZITSANI
ZOLIMBIKIRA NTCHITO.




A man with a long, dark beard and mustache, wearing a brown and yellow striped tunic, is shown from the chest up. He is holding a long, wooden staff or spear with both hands. The background is a plain, light-colored wall.

YHOVA,
KUCHOKERA
NTHAWI IMENE
NDINAYAMBA
KUYANKHULA
M'DZINA LANU,
ZINTHU
ZIKUPIRAPIRABE.
NCHIFUKWA
CHIYANI
MWANDITUMA
KUNO?


INE NDINE YHOVA,
MULLINGU WA MAKOLO AKO,
ABRAHAMU, ISAKE,
NDI YAKOBO.

■
NDAONA KUZUNZIKA
KWA ANTHU ANGA
AISRAELE NDIPO
NDAMVA KULIRA KWAO.
// NDI NTHAWI YOTI
NDIKWANIRITSE
PANGALO LANGA KWA
ABRAHAMU NDI
KUWATULUTSA
ANTHUWA KUTI APITE
KU DZIKO LA KANANI.
IWEYO, MOSE,
UDZAWATULUTSA.



KOMA SINDITHA
KUYANKHULA. FARAO
SADZANDIMVERA.

AARONI NDIYE
AZIDZAYANKHULA; IWE
UZINGOMVETSERA KWA
INE NDIPO UZIMUUSA ZOTI
ANENE. POYAMBA,
FARAO SADZAKUMVERA,
KOMA NDIDZAMUONETSA
ZIZINDIKIRO ZAZIKULU
KUFIKIRA AIGUPTO
ADZADZIWA KUTI
INE NDEKHA NDIYE
MULLUNGU WOONA.



HA, HA,
MUKUDZACHITANS
O CHIYANI KUNO?

YHOVA AKUTI,
"LOLA KUTI
ANTHU ANGA
AMUKE."

ICHI NDI
CHIZINDIKIRO CHIMENE
YEHOVA WAYANKHULA.

HA-HA-HA, ZIMENEZI
NZAMATSENGA CHABE.
SIZINGANDIOPSEZE
MPANG'ONO POMWE.
ITANANI AMATSENGA
ATHU.

ANACHITITSA
KUTI TSENGALO LIONEKE
NGATI ZENIZENI.

ADAPHUNZIRA
KUTI ZIMENEZI?




**BWERETSANI
MSANGA TSENGA
LIJA LIMACHITITSA
KUTI NDODO ZANU
ZISANDUKE NJOKA.**



MULUNGU WATHU WA
NJOKA, NESERITI,
WATITUMA KUTI TIKUUZENI
KUTI MUZIUMBA NJERWA
ZAMBIRI. HA, HA, HA.





MOSE, TICHITE
CHIYANI TSOPANO?
AKUTIONA NGATI
OPLUSA?

EKSODO 7:11-12




ONANI!
NJOKA YAKE
IFUNA
KUMENYANA NDI
ZATHU.



**NJOKA YAKE
IKUDYA
IMODZI MWA
NJOKA
ZATHU!**



**YAMEZERATU
NJOKA YATHU!**



KOMA SINGADYENSO
YACHIWIRI! MULUNGU
WATHU WA NJOKA,
NESERITI, ADZAKWIYA.



YEHOVA
NDIMULLINGUA
MENEADALENG
A ZONSE.
AKUTI,

ZIMENEZI
ZATHEKA
BWANJI?



**YHOVA NDI
MULLUNGU AMENE
ADALENGA ZONSE.
AKUTI, "LOLA KUTI
ANTHU ANGA AMUKE."**

EKSODO 7:12

**SINDIKUDZIWA MMENE
UNACHITIRA ZIMENEZI, KOMA
SINDINGALOLE KUTI AKAPOLO
ANGA AMUKE CHIFUKWA CHAKUTI
IWEYO WACHITA ZA MATSENGA.
CHOKANI!**



**EKSODO 7:13 "KOMA MTIMA
WA FARAO UNALIMBA,
NDIPO SANAMVERA
IWO MONGA, MONGA
ADALANKHULA YEHOVA."**

NCHIFUKWA CHIYANI
YEHOVA ANATITUMA KUNO
KUDZACHITA ZIZINDIKIRO ZOMWE
AMATSENGA A FARAO AMACHITANSO?
POPEZATU TINAONEKA NGATI
OPUSA.



SINDIKUDZIWA, KOMA
MULLUNGU ADZAUMITSA MTIMA WA
FARAO. NDI ZOONA. KODI UNAONA
MMENE ANACHITIRA MISALA
PAMENE NJOKA YATHU INKADYA
TINJOKA TAKE?

NDIYENERA
KUPEZA MALO OTI
NDIYANKHULIRE
NDI YEHOVA.
SINDIKUDZIWA KUTI
TICHITE CHIYANI
TSOPANO.

MULUNGU
ANAKUMANANSO
NDI MOSE
NAMUZA ZOTI
ACHITE. AIGUPTO
ANAMUSEKA MOSE.
ANTHU AKENSO
ANAMUKANA
CHIFUKWA FARAO
ANAWAWITSA
UKAPOLO WAO,
KOMA MOSE
ANAKHULUPIRIRABE
MULUNGU
NKUMAMUMVERA
NGAKHALE KUTI
SANKAMVETSA
ZIMENE MULUNGU
ADAMTUMIRA.



**YEHOVA AKUTI, "POPEZA
SUKUFUNA KUTI ANTHU ANGA
AMUKE, TSONO KUTI UDZIWE
KUTI INE NDINE MULUNGU
WOONA, MADZI ONSE A MU
MTSINJE WA NAILO
ADZASANDUKA MAGAZI.**




TSOPANO
IZI NZOOPSA.
ANACHITA
BWANJI
ZIMENEZI?

TAKATENGANI
AMATSENGA ANGA.
MULUNGU WA NAILO
ADZALETSA ZIMENEZI.



ONANI? AMATSENGA
ANGA AKHOZANSO
KUCHITA ZIMENEZI.
SINDIDZAGONJA
CHIFUKWA CHA MATSENGA
ANU ABODZAWO.



PA MOYO
WANGA WONSE
SINDINAONEPO ZOTERE.
NGAKHALE TIMIFULENI NDI
TIMADZIWE TING'ONOTING'ONO
TASANDUKA MAGAZI. KODI
AMATI MULUNGU WAKE DZINA
LAKE NDANI?

SINDIDAWAMVEPO AKUTCHULA
DZINA LA MULUNGU WAO. PALI
KUSIYANA KWANJI? IFE TILI NDI
MILUNGU ZIKWIZIKWI. MULUNGU
WA MTSINJE WA NAILO AYENERA
KUTI WAKWIYA KWAMBIRI.



MULLUNGU
MMODZI?
ZOSEKETSA
NDITHU.

MOSE AKUTI
MULLUNGU WAKE
NDI MMODZI
YEKHA.

PATATHA MASIKU 7
MADZI ATASANDUKA
MAGAZI, MOSE
AKUBWERETSANSO
CHILANGO CHINA
CHA MULUNGU
PA AIGUPTO.



MADZI
ABALE ACHULE
AMBIMBIRI.

MADZI ONUNKHA A
MAGAZI AJA ANABALA
ACHULE OSAWERENGEKA.



EKSODO 7:21-25, 8:6




NYUMBA
YANGA
YADZALA NDI
ACHULE.

DZIKO LONSE
LA IGUPTO
LADZALA NDI
ACHULE. MILINGU
YAKWIYA!

KODI ALI KUTI
ANSEMBE ATHU?
KODI
SANGACHITEPO
KANTHU?




EYIIII!



NCHIFUKWA CHIYANI
AKULENGA ACHULE? KODI
ACHULE AMENE MOSE
WATIPATSA SADAKWANIRE?
TSOPANO FARAO
AKUTIONJEZERA ENA.

FARAO,
TAMVERANI,
IFE AMATSENGA
TIKHOZANSO
KULENGA ACHULE.

BWANJI OSAWALOLA
KUTI APITE M'CHIPULULU
MONGA MOMWE AKUFUNIRA?
SITINGAPIRIRE NDI IZI.



ITANITSIRENI
MOSE, MUMUZE
KUTI NDILI NDI
MAU.

INDE BWANA,
NDICHITA MONGA
MWANENERA.




UMUPEMPHE YEHOVA KUTI
ACHOTSE ACHULEWA. AKATERO,
NDIDZALOLA KUTI ANTHU AKO
APITE M'CHIPULULU
KUKAPEREKA NSEMBE.

UTCHULE NTHAWI
IMENE UFUNA KUTI
ACHULEWA AFE NDIPO
ZIDZACHITIKADI.

MAWA
MMAWA.


ZIDZACHITIKA MONGA
MWA MAU AKO, KUTI NONSE
MUDZIWE KUTI PALIBE
MULUNGU WOFANANA
NDI YEHOVA.



FARAO ATAONA
KUTI ACHULE AFA
PA NTHAWI IMENE
ADAANENA,
ADALUMITSA MTIMA
WAKE NDIPO
SADALOLE KUTI
AHEBRI AMUKE.

KODI YEHOVAYU NDI MULUNGU
WOTANI, AMENE WADZAZA
DZIKO LATHU NDI ACHULE?

NCHIFUKWA CHIYANI
UKUGANIZA KUTI NDI
MULUNGU AMENE ADACHITA
ZIMENEZI? MWINA MWAKE
ZANGOCHITIKA BASI.



NANGA MOSE
ADADZIWA BWANJI KUTI
ZIDZACHITIKA MOTERE?
NANGA ADADZIWANSO
BWANJI NTHAWI YENIYENI
YOMWE ADZAFERE?

KHALA CHETE,
FOSHOLO
M'MANJA, KUTI
TIMALIZE
MWACHANGU.




NDIPO YEHOVA ANATI KWA MOSE, "UWUZE AARONI, TAMBASULA DZANJA LAKO NDIPO UMENYE NTHAKA YA PA DZIKO KUTI FUMBI LISANDUKE NSABWE M'DZIKO LONSE LA IGUPTO."

NDIPO FUMBI LONSE
M'DZIKO LA IGUPTO
LINASANDUKA NSABWE.



EEEE!



MUKUTANTHAUZA CHIYANI
MUKAMATI SIMUNGAPANGE
NSABWE? ANTHU ADZAGANIZA
KUTI MULUNGU WAKE
NGWAMPHAMVU KUPOSA MILUNGU
YATHU! MUYENERA KUCHITA
ZAMATSENGA BASI.

KOMA BWANA, NTCHITO
AKUCHITA ANZATHUWO NDI YA
MULUNGU. PALIBE AMENE
ANGACHITE ZIMENE ANTHU
AWIRIWO AKUCHITA. TILIBE
MPHAMVU.



PAFUNIKA KULONGOSOLA BWINO
ZIMENEZI POTSATA CHILENGEDWE, KOMA
SITINGAPIRIRE NAZO ZIMENEZI. PITANI
KWA MOSE. MUKAMUUZE KUTI MULUNGU
WAKE AKACHOTSA NSABWEZI NDIDZALOLA
KUTI AHEBRI AMUKE KUTI AKATUMIKIRE
MULUNGU WAO.



NSABWE ZACHOKA,
KOMA SINDINGALOLE
KUTI AKAPOLOWO
AMUKE. KODI MULLUNGU
WAKE ANGACHITENSO
CHIYANI?



**MULUNGU WAYANKHULA
NDI MOSE. MULUNGU AKUTI,
"NDIDZATUMIZIRA AIGUPTO
MIZAZA. NYUMBA ZANU
ZIDZADZALA NDI MIZAZAYO.
KOMA PANO
NDIDZASIYANITSA PAKATI
PA AIGUPTO NDI AHEBRI.**

**KOMWE KUMAKHALA
ANTHU ANGA
SIKUDZAKHALA MIZAZA.
CHIFUKWA CHA
CHIMENECHI ALIYENSE
ADZADZIWA KUTI INE
NDINE MULUNGU WA
DZIKO LONSE
LAPANSI."**

ABABA, NCHIFUKWA
CHIYANI ANSEMBE ATHU
SAKUMULETSA MUNTHU
AMENEYU? MPHAMVU
ZAO ZILI KUTI?



SINDIDZIWA
CHILICHONSE
CHOKHUDZA NKHANI
ZA CHIPEMBEDZO.
INE NDIMANGOSAMA
ZANGA BASI.



PITANI
KWA
MOSE.


ZILI MONGA MUJA
ADANENERA; KULIBE MIZAZA
KWA AHEBRI! ZIMENEZI
AKUCHITA NDI MULLUNGU
WAO NDITHU.



PITANI, KAPEREKENI
NSEMBE KWA MULLUNGU
WANU, KOMA MUSACHOKE
M'DZIKO LA IGUPTO.

TIYENERA
KUPITA ULENDU
WA MASIKU
ATATU.


NDINATI MUKHOZA
KUPITA, KOMA MUSAPITE
KUTALI KWAMBIRI. TSOPANO
YANKHULA NDI MULLUNGU
WAKO NDIPO UMUPEMPHE
KUTI ACHOTSE MIZAZA
YONUNKHAYI.



PALIBE NDI
MZAZAUMODZI WOMWE
UMENE WATSALA M'DZIKO
LA IGUPTO. CHIMENECHI
NCHODABWITSA
NDITHU.

KHALA CHETE.
LUKUKHALA NGATI UFUNA
KUKHULLUPIRIRA
MBUTUMAYO.

FARAO ADAUMITSANSO
NTIMA WAKE NDIPO
SADALOLE KUTI
ANTHUWO AMUKE.




MULLINGU ANATUMIZIRANSO
AIGUPTO MLIRI WINA: NG'OMBE
ZAO ZONSE, NKHOSA, AKAVALO,
NDI NGAMIRA ZIDAGWIDWA NDI
MATENDA A ZILONDA NDIPO
ZINAFU. KOMA ZIWETO ZA AHEBRI
ZIZIDAGWIDWE NDI MATENDAWO.

ZIWETO ZATHU
ZONSE ZAFU KOMA
ZANU ZILI BWINOBWINO.
TATILUZANI CHIFUKWA
CHAKE.

MOSE AKUTI NDI
CHIFUKWA CHA MULLINGU
WATHU AMENE WABWERA
KUDZATIOMBOLA KU
UKAPOLO WANKHANZAWU,
KOMU INE NDINE MUNTHU
WAMBA CHABE,
SINDIZIDZIWA ZINTHU
ZOTEREZI.



ANSEMBE ATHU
AKUPEREKA NSEMBE KWA
MILINGU YATHU. NG'OMBE
YATHU YOPATULIKA IKWIYA
NDIPO ITHETSA ZIMENE
ZIKUCHITIKAZI.




MUMUZE FARAO KUTI
WACHEDWA. NG'OMBE ZATHU
ZONSE ZOPATULIKA ZINAFU. ANTHU
AKWIYA KWAMBIRI AKAMVA KUTI
MILINGU YATHU SINAWAPULUMUTSE
KWA MILINGU WANKHANZA
WA AHEBRIWA.

KODI MILINGU
YA IGUPTO ILI
KUTI? KODI ILIBE
MPHAMVU?

KOMA FARAO
ADALIMITSABE
MTIMA WAKE.

EKSODO 9:6-7

MULLINGU
ANAYANKHULANSO NDI
MOSE KUTI AWAZE
PHULISA PAMWAMBA PA
MZINDA, NDIPO AIGUPTO
ADZATULUKA ZITHUPSA
M'THUPI MWAO MONSE.




MULLINGU AKUTI,
"POPEZA SUKULOLA KUTI
ANTHU ANGA AMUKE,
NDIDZATUMIZA ZITHUPSA
PA INU NDI PA ZIWETO
ZANU ZONSE."

AI, ZIMENEZI
ZISACHIKIKE
NSO.


**ITANANI AMATSENGA.
AUZENI KUTI
ASONKHANITSE MPHAMVU
ZAO. APEREKE NSEMBE
KWA MILUNGU KUTI IZI
ZISACHITIKE.**





MUNAITANA,
INU
WOPAMBANA
KOPOSA?

KODI NAWENSO
ULI NDI ZITHUPSA?
KODI ULIBE MPHAMVU
ZOTSUTSIRAMULINGU
WA MOSEYU?



CHOKERENI, INU ANTHU
ACHABECHABE, OPANDA NDI
MPHAMVU ZOMWE.
MUMANGOPUSITSA ANTHU BASI,
KOMA NDIMADZIWA KUTI NDINU
ACHINYENGO. MILINGU
YANU ILI KUTI?

**MULAWIRIRE MMAWA KWA FARAO KUKAMUUSA KUTI,
"MULUNGU WA AHEBRI AKUTI, 'ULOLE ANTHU ANGA AMUKE.
DZIWA KUTI MLIRI UMENE UKUBWERA UDZAKHALA WOOPSA
KOPOSA. CHIONONGEKO CHIMENE CHIDZABWERE NDI
MLIRIWO CHIDZAPHA ANTHU AKO AMBIRI. CHIFUKWA CHA
CHIMENECHI UDZADZIWA KUTI KULIBE MULUNGU WINA
WOFANANA NANE. SUZINDIKIRA, KOMA NDINE AMENE
NDINACHITITSA KUTI UKHALE FARAO.**



**LIWUMA LAKOLI NDILO LACHITITSA
KUTI NDIWONETSE MPHAMVU ZANGA
NDI KULANGA AEJIPITO CHIFUKWA
CHOZUNZA ANTHU ANGA. UKUNGOSAMALA
ZAKO, NDIPO UKUKANA KUCHITA CHIFUNIRO
CHANGA, TSONO MAWA NTHAWI NGATI
YOMWE INO NDIDZATUMIZA MATALALA
NDI MOTO, ZIMENE SIZINACHITIKEPO
PA DZIKO LAPANSI."**





**NDIKUKUUZANI KUTI MUDZIWITSE
ANZANU KUTI MUDZISAMALIRE PAMODZI
NDI ZIWETO ZANU, SIMUYENERA
KUTULUKA M'NYUMBA ZANU, ZIWETO
ZANUNSO ZISATULUKE M'KHOLA,
POPEZA CHILICHONSE CHIMENE
CHIDZATULUKA CHIDZAFU."**



ZIKHALE
MONGA
YEHOVA
WANENERA.




AAAAA.

**ZIMENEZI
ZINGATHEKE
BWANJI, MOTO
NDI MATALALA
KUPHATIKIZANA?**

***SETI MULLUNGU
WAMPHAMVU,
TIPULUMUTSENI.***

**ONSE AMENE SANASAMALE
CHENJEZOLI, NATULLUKA
M'NYUMBA ZAO ANAFA.**




ABABA, MOSE UJA
WACHITA BWANJI ZIMENEZI?
KODI MULLINGU WAKE NDI
WAMPHAMVU KUPOSA SETI,
MULLINGU WA ZOOPSA NDI
MAFLUNDE?


IYE AMATI
KULI MULLINGU
MMODZI YEKHA,
NDIPO KUTI
AHEBRI NDI ANA A
MULLINGUYO.



KOMA PALIBE AMENE ADAONAPO
MULLINGU WAKEYO, NGAKHALE AHEBRIWO
SANAMUONEPO. MULLINGU WAKE AMENE
AKUNENAYO NDI MZIMU. NDIPO MOSE
AKUNENA ZA MULLINGUYU POFUNA
KUKAKAMIZA FARAO KUTI AWALOLE KUPITA
KU CHIPULULU KUKAPEMBEDZA.



SETI MULLINGU WAMPHAMVU,
MBUYE WA ZOOPSA NDI MAFUNDE,
THETSANI MAFUNDE OONONGAWA.
ZOONA ZAKE NZAKUTI INU NDINU
WAMKULU KUPOSA MULLINGU
WOSAONEKA WA MOSE.




ZIMENEZI SIZIYANDIKIRA
IFE - KOMA AIGUPTO
OKHA.

ABABA, NDIKUOPA.
KODI MATALALA NDI
MOTOWO ZIGWERANSO
IFE?

AI MWANA WANGA,
YHOVA AKULANGA AIGUPTO
CHIFUKWA CHOSAMUMVERA.
AKUWAONETSA KUTI SETI,
MULLINGU WAO

NDI
ZOOPSA
KWAMBIRI.



NDACHIMWIRA YEHOVA.
MULLINGU WA AHEBRI NDI
WOLUNGAMA, KOMA INE NDI
ANTHU ANGA NDIFE OCHIMWA.
UPEMPHE YEHOVA KUTI ALETSE
MATALALA NDI MOTOWU, NDIPO
NDIDZALOLA KUTI ANTHU AKO
AMUKE MWANSANGA.

NDIKANGOTULLIKA MU MZINDA
MUNO NDIDZAKWEZA MANJA ANGA
KUMWAMBA NDIPO MLIRIWU ULEKA.
CHIFUKWA CHA CHIMENECHI
LIDZADZIWA KUTI DZIKO LAPANSI NDI
LA YEHOVA, KOMA SUDZASUNGA MAU
AKOWA, CHIFUKWA SUNAYAMBE
KUOPA YEHOVA.

ATAONA KUTI MLIRI UJA
WALEKA, FARAO
ANACHIMWIRANSO
MULLINGU POUIMITSABE
MTIMA WAKE. SADALOLE
KUTI ANTHUWO AMUKE.



MULINGU ANATUMIZANSO MLIRI
WINA. DZOMBE LINADZA NDI
KUDYA CHOMERA CHILICHONSE
CHIMENE MATALALA AJA
SANAONONGE. KENAKA DZOMBE
LIJA LINAYAMBA KULOWA
M'NYUMBA ZA ANTHU.


EKSODO 9:26-35, 10:13-15



AMAMA-
MAMA

AAAAAA!

TENGA
ICHO!



GEBU, MULLINGU WA
ZOMERA, KODI SIMUKUONA
ZIMENE MULLINGU WA
AHEBRI AKUCHITIRA
MBEU ZATHU.


OSIRISI, LERO
ONETSANI KUTI
NDINU AMPHAMVU.

FARAO ANAITANA MOSE NALONJEZA KUTI
ADZALOLA KUTI ANTHUWO AMUKE, KOMA
PAMENE MULLINGU ADACHOTSA DZOMBE
LIJA, FARAO ANAUMITSANSO MTIMA NDIPO
SANALOLE KUTI AKAPOLOWO AMUKE.



KENAKA MULLINGU ANACHITITSA KUTI MUKHALE
MDIMA WANDIWEYANI M'DZIKO LA AIGUPTO.
KWA MASIKU ATATU KUNALI MDIMA WOOPSA,
KOMA KUMALO KUMENE AHEBRI ANKAKHALA
KUNALI KOWALA.

NDIKADAKUPHA
KALE POFIKA LERO,
KOMA CHIMENECHO
CHIKUWONETSA KUTI
MULLINGU WAKO NDI
WAMPHAMVU
KUPOSA MILLINGU
YATHU.




SINDIDZAONANSO
NKHOPE YAKO,
POPEZA PA TSIKU
LIMENELO UDZAF A.

WAYANKHULA
CHOONADI LERO LINO.
ZONADI
SITIDZAONANANSO.



RA, MULLINGU
WAMKULU WA DZUWA,
TIMVERENI. MWABISALA
KWA MASIKU ATATU. KODI
SIMUNGAMGONJETSE
MULLINGU WA AHEBRIYU?




TAMVERANI! KWATSALA MLIRI UMODZI
NDIPO FARAO ADZAKONDWA PAMENE TIZIDZATULLIKA
MU IGUPTO. USIKU UNO, MNGELO WOONONGA
ADZADUTSA M'DZIKO LA IGUPTO. M'BANJA LILILONSE
ANA AAMUNA OYAMBA KUBADWA ADZAFI. MULLINGU
ADZALANGA OCHIMWA USIKU UNO.

KOMA NANGA
ANA ATHU OYAMBA
KUBADWA? KODI
NAWONSO ADZAFI?




MULLINGU WAKONZA
ZOPULLUMUTSA ONSE
AMENE AMAMKHULLUPIRIRA,
KUPHATIKIZAPO AIGUPTO.
PITANI TSOPANO KATENGENI
MWANA WA NKHOSA
WAMWAMUNA KAPENA WA
MBUZI, MUMUPHE NDIPO
MAGAZI AKE MUWAPAKE
MBALI ZONSE ZIWIRI ZA
ZITSEKO ZANU.

EKSODO 10:22-29, 11:4-5, 12:3-7




**YHOVA AKUTI, "NDIKAMAYENDA M'DZIKOLI
USIKU UNO, KUPHA ANA ONSE AAMUNA OYAMBA
KUBADWA, NDIKAONA MAGAZI KUNJA KWA ZITSEKO
ZANU, NDIDZADUTSA NYUMBA IMENEYO, NDIPO
ANA OYAMBA KUBADWA SADZAFI M'MENEMO.
MUKHALE M'NYUMBA ZANU USIKU UMENEWU
NDIPO MUZIDYA MWANA WA NKHOSA
AMENE MUPHEYO."**



TSOPANO PITANI KWA
MABWANA ANU ACHIIGUPTO,
MUKABWEREKE ZINTHU ZAO
ZAMTENGOWAPATALI, GOLIDE,
ZOKONGOLETSERA, NDI SILIVA.
MULLINGU WAKHUDZA MITIMA
YAO. ADZAKUPATSANI ZAMBIRI
MOWOLOWA MANJA.//
MULONGEZE KATUNDU WANU
NDIPO MUKHALE OKONZEKA
KUNYAMUKA MAWA MMAWA.




SIMUDZABWERERANSO KUNO. KUMENKO
NKUTSAZIKANA NAYE IGUPTO MPAKA
KALEKALE. CHIMENECHI CHIDZAKHALA
CHIYAMBI CHA NTHAWI YANU - NDILO TSIKU
LANU LOYAMBA.



ABABA, PAJATU
NKHOSA YATHU NDI
YOMWEYI, KODI
SITINGAGWIRITSE
NTCHITO UTOTO
WOFIIRA?

MWANA WANGA, MULLINGU
ANATI TIPHE MWANAWANKHOSA
NDI KUPATA MAGAZI AKE
PAMPHUTHU PA ZITSEKO ZATHU.
TIYENERA KUCHITA MONGA
ANANENERA. WAONA MMENE
AMAWERUZIRA ANTHU AMENE
SAMUMVERA. NKHOSA
IDZAKUPULUMUTSA KU IMFA.

A woman with dark, curly hair, wearing a headwrap and a patterned top, is shown in a close-up. She is holding a small, light-colored animal, possibly a rabbit or a small dog, in her hands. The background is a solid orange color. There are two speech bubbles containing text in Swahili.

NDIYE KUTI
MWANAWANKHOSA
YU WAFU M'MALO
MWANGA?


INENSO WANDIFERA.
PAJATU INENSO NDINE
MWANA WAMWAMUNA
WOYAMBA KUBADWA
KWATHU.



**YEHOVA ANATI,
NDIKADZAONA MAGAZI
PA ZITSEKO ZANU
NDIDZADZIWA KUTI
MUMANDIKHULLUPIRIRA
NDIPO SINDIDZAPHA
ALYENSE
M'NYUMBAMO.**


**AMAI, NCHIFUKWA
CHIYANI ABABA
AKUPAKA MAGAZI
PA CHITSEKO?**

EKSODO 12:26-28, 35-36

A comic book panel depicting a scene inside a wooden building. On the left, a man with a beard and a headband is seen from the back, looking towards the right. On the right, a woman in a green dress is talking to a young boy. The woman has a slightly annoyed or questioning expression, while the boy looks up at her with a curious or pleading expression. The background shows wooden walls and a window with a lattice pattern.

NCHIFUKWA CHIYANI
SIMUNAPHE
MWANAWANKHOSA
NDI KUPAKA MAGAZI
AKE PA CHITSEKO
CHANU?

HA, KODI NAWENSO
UMAKHULUPIRIRA ZACHACHABEZI?
KODI MAGAZI ANG'ONONG'ONO A
PA CHITSEKO ANGALETSE BWANJI
IMFA? MWANA WANGA
SAKUTEKESEKA. KODI PAJA DZINA
LAKO NDI YOIKIMU?



AI SIZINGATHEKE.
KODI MUKUGANIZA
KUTI NDINE OPLUSA?
ANTHU OPEPERA
NDIWO AYENERA
KUMAPEMBEDZA.

MULLINGU WABWINO SANGAPHE ANTHU
CHIFUKWA CHOLEPHERA KUPAKA MAGAZI
ANG'ONO'NG'ONO PA CHITSEKO. NANGA
ANTHU AMENE SADAMVE ZIMENEZI?




ABABA, NCHIFUKWA
CHIYANI USIKU WA LERO
UKUSIYANA NDI USIKU
WINA WONSE
M'MBUYOMU?

NCHIFUKWA CHAKUTI
USIKU WA LERO YEHOVA
ADZATUMIZA MNGELO
WOONONGA KUDZAPHA ANA
AAMUNA ONSE OYAMBA
KUBADWA AMENE
SAKHULLUPIRIRA IYE. KOMA
AKAONA MAGAZI, ADZADUTSA
NYUMBA IMENEYO.




'PASKHA' NDI MAU
ACHIHEBRI,
KUTANTHAUZA
KUTI, 'KUDUTSA'
KAPENA
'KULAMBALALA.

CHIMENECHI NDICHO CHIYAMBI
CHA MASIKU KWA IFE. CHAKA CHILICHONSE
NTHAWI NGATI IMENEYI TIZIDZACHITA
CHIKONDWERERO CHA PASKHA,
KUKUMBUKIRA KUTI MULUNGU
ADATIPULUMUTSA M'DZANJA LA FARAO.



ABABA, MVERANI
KULIRAKO! NKUTHEKA
KUTI MNGELO
WOONONGAYO ALI
M'DERA LINO.

USAOPE. IFE
TAMVERA MULUNGU.
MAGAZI ALI PAMPHUTHU
PA CHITSEKO. TIKUDYA
MWANAWANKHOSA.



**MWANA WANGA
WAMWAMUNA
WAMWALIRA. MULUNGU,
THANDIZENI. ITANANI
MOSE.**

EKSODO 12:28



I!!!!

MAYOOOO!

**AI,
AMBUYE!
MWANA
WANGA AI!**



PAMENE MNGELO WOONONGA ANKAYENDA
MUMZINDAMO USIKU UMENEWO, ANTHU
ZIKWIZIKWI ANAPHEDWA. AMENE
ADAKHULUPIRIRA NAPAKA MAGAZI PA
ZITSEKO ZAO ANAKHALA NDI MOYO.



PEPANI, KOMA MWACHEWA.
MUDACHENJEZEDWA, KOMA
SIMUNAFUNE KUKHULUPIRIRA.
CHOMVETSA CHISONI NCHAKUTI
AMBIRI AFA USIKU UNO.



**MWANA WATHU
WAMWAMUNA
WAMWALIRA!**

**FULLUMIRA, ITANA
MOSE ABWERE
KUNO MSANGA.**



CHACHITIKA
NCHIYANI?


**NDI
MWANA
WOYAMBA
KUBANJA
KWAO!**

EKSODO 12:29-31



FARAO
ANAITANITSANSO
MOSE.

KOMA FARAO SANAYANG'ANE
NKHOPE YA MOSE.



NDACHIMWA.
CHONDE CHOKANI MU
MU IGUPTO MUNO, IWE
PAMODZI NDI AHEBRI
ONSE. YEHOVA NDI
MULLINGUWOPAMBANADI.
KOMA LUNDIDALITSE
USANACHOKE.



MONGA MOMWE MULLINGU ANALONJEZERA
MAKOLO AO, PATATHA ZAKA 400, AISRAELI
ANATULLIKA MU IGUPTO. AIGUPTO ANAPEREKA
KWA AHEBRI GOLIDE, ZOKONGOLETSERA, NDI
CHAKUDYA, NDI CHILICHONSE CHIMENE AKANATHA
KUNYAMULA PA ULENDO WAO. NTHAWI IMENEYO
AHEBRI ANASANGALALA KWAMBIRI; POPEZA LINALI
TSIKU LOYAMBA LA FUKO LATSOPANOLO.

AMUNA 600,000,
PAMODZI NDI AKAZI NDI
ANA, ANATULUKA MU
IGUPTO KUPITA KU DZIKO
LAMALONJEZANO.

EKSODO 12:21-22, 31-38



MASANA MULLINGU ANKAWATSOGOLERA
NDI MTAMBO, UMENE LINKAWAPATSA
MTHUNZI, NDIPO USIKU ANKAWATSOGOLERA
NDI MOTO, UMENE LINKAWALNIKIRA.



<https://goodandevilbook.com/>